

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

ANAMWALI KHUMI

(Mateyu 25:1-13)

Yesu ananena fanizo logwira mtima kwambiri la anamwali khumi, pofuna kuphunzitsa za kukonzekera kwauzimu komwe kumachititsa kuti munthu udzifufuze mkati mwako. Kubwera kwachiwiri kwa Khristu kukufaniziridwa ndi mwambo waukwati, kumene Yesu monga, mkwati adzabweranso kudzalandira mkwatibwi wake, umene uli mpingo. Cholinga cha fanizoli ndicho kutichenjeza kuti tikhale maso ndipo tikonzekere kubweranso kwa Khristu.

Anamwali khumi, yense atanyamula nyali, anatuluka kukakomana ndi mkwati. Asanu mwa iwowa akunenedwa kuti anali ochenjera, pamene ena asanu akutchedwa opusa. Kusi yana kwakukulu pakati pa magulu awiriwa kunali mu kukonzekera kwao popeza anamwali ochenjera anabweretsa mafuta oonjezera mu nyale zao, pamene opusa sanatero. Pamene anali kuyembekezera mkwati amene anachedwa, anamwali khumiwo anatopa ndi kugona. Pakati pa usiku, mwadzidzidzi kunamveka mfuu yakuti: “Onani, mkwati! Tulukani kukakomana naye.”

Atadzutsidwa, anamwaliwo anagwedeza nyale zao kuti ziyake bwino. Anamwali opusawo anazindikira kuti nyali zao zinali zitazima chifukwa munalibe mafuta. Iwo anachita mantha, napempha anza ochenjerawo kuti awagawireko mafuta. Anamwali ochenjerawo anali ndi mafuta okwanira iwo eni ndipo anauza anamwali opusawo kuti apite akadzigulire mafuta.

Pamene anamwali opusa aja anapita kukagula mafuta, mkwati anafika. Iwo amene anali okonzeka—anamwali ochenjera—analowa naye limodzi muphwando laukwati, ndipo

chitseko chinatsekedwa. Pamene anamwali opusawo anabwerera, anachonderera kuti alowe, nati, “Mbuye Mbuye, mutitsegulire ife.” Mkwatiyo anayankha kuti: “Indetu ndinena kwa inu, sindikudziwani.”

Yesu anamaliza fanizoli ndi chenjezo lomvetsa chisoni lakuti: “Chifukwa chake dikirani, pakuti simudziwa tsiku lake, kapena nthawi yake imene Mwana wa munthu adzadza.” Chenjezoli likutsindika kufunika kokhala ndi moyo wokonzeka nthawi zonse pamene tikuyembekeza kubweranso kwa Khristu.

Kuti titanthauzire molondola tanthauzo la fanizoli, mpofunika kuzindikira kuti si mfundo zonse zomwe zimaperekedwa kuti zipereke choonadi cha chiphunzitsa. Mafanizo ndi nkhani zomwe zimapereka phunziro lalikulu, zomwe zimakhala ndi zina zoonjezera kuti zitithandizire kumvetsetsa koma osati kuimira choonadi chenichenicho. Pamene, anamwali khumiwo sakuimira osakhulupirira koma anthu amene amadzinena kuti ndi a makhalidwe abwino, opanda banga ku dziko, ndi otsatira a Mulungu.

Kugawanikana pakati pa anamwali ochenjera ndi opusa sikukutanthauza kuti theka lokha la iwo odzitcha Akhristu ndiwo adzapulumutsidwe; m'malo mwake, zili ngati chenjezo kwa Akhristu onse kuti adziyang'anire pa makhalidwe ao auzimu. Pamene anamwaliwo anali kuyembekezera, ndi anzeru okha amene anakonzekera kufika kwa mkwati.

Pamene mkwati anachedwa, anamwaliwo anatopa ndi kugona. Izi zili zofanana ndi kutopa kwauzimu ndi kumasuka kumene kumayamba pamene Akhristu akuyembekezera kubweranso kwa Khristu. Dziko ladzala ndi

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Koma pakati pa usiku panali kufuula, Onani, mkwati! Tulukani kukakomana naye.”

Mau a Mkonzi

Kalozera pophunzira
Baibulo: Chilungamo

Zovala za Chilungamo

Funso Yanko

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

zosamalira, zododometsa, ndi mayesero. Kuchedwa kwa kubwera kwa Khristu kungayambe kupangitsa kusalabadira pokonzeka mwauzimu. Anamwali opusa, poyembekezera kuti mkwatiyo afika msanga, sanakonzekere mokwanira ndi kunyalanyaza kubweretsa mafuta okwanira mu nyale zao. Mafutawa akuimira kupezeka kwa Mzimu Woyera m'moyo wa wokhulupirira.

Anamwali ochenjerawo anakonzekera nanyamula ndi mafuta okwanira kuti nyali zao ziziyaka. Iwo anali ndi ubale wosasunthika komanso weniweni ndi Mulungu, wosungidwa mwa Mzimu Woyera.



Chikhulupiriro chao sichinali chakunja kokha chongoonetsa ntchito zaumulungu koma chinali chozikidwa mozama mu mphamvu yochirikiza ya Mzimu Woyera, imene inawapangitsa iwo kuwala m'dziko lamdima.

Pamene mkwati anafika, anamwali ochenjera anali okonzeka ndipo analandiridwa kuphwando laukwati. Phwando laukwati likuimira chiyanjano chomaliza pakati pa Khristu ndi mpingo wake kumapeto kwa nthawi. Chitseko chitangotsekedwa, panalibenso mwai

woti opusa aja alowe. Izi zikuimira kumalizika kwa chiweruzo pa kubweranso kwa Khristu. Yesu akadzabweranso, sipadzakhala nthawi yopemphera, kufunafuna chitsitsimutso, kuyeretsewa, kapena kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu. Sipadzakhala mwai wachiwiri.

Chimodzi mwa zinthu zochititsa chidwi kwambiri m'fanizoli ndi kuyankha kwa mkwati kwa anamwali opusa aia kuti: "Sindikudziwani." Izi zikuonetsa kuopisa kwa kudalira maonekedwe akunja achikhulupiriro opanda mzimu weniweni. Ngakhale kuti anamwali opusawo ankaoneka kuti akuyembekezera mkwati, iwo anali osakonzekera ndipo analibe ubale weniweni ndi Mulungu. Iwo anali nao maonekedwe aumulungu koma analibe moto weniweni wa Mzimu wa Mulungu.

Wokhulupirira aliyense adziyese kukonzeka kwake kwa uzimu. Kodi uli mgulu la ochenjera kapena la opusa? Kodi muli ndi mafuta a Mzimu Woyera m'moyo wanu, kapena mukudalira machitidwe achipembedzo akunja? Ha!, iwe moyo wosamalala, dzuka ku tulo taulimu ndi kukonzekera kubweranso kwa Ambuye.

Uthengawu ndi womveka: dikirani ndipo khalani okonzeka, pakuti palibe amene akudziwa kuti Khristu adzabwera liti. Ino ndi nthawi yokonzekera. Ngati simunadzazidwe ndi moto woyaka wa Mzimu Woyera m'moyo wanu, musachedwe. Khomo la mwai lili lotsegula lero, koma silidzakhala lotseguka kwamuyaya. Kuitana komaliza kudzafika, chitseko chidzatsekedwa.

Kodi mwakonzeka kukumana ndi mkwati? Ino ndiye nthawi yake! ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Chilungamo chikuza mtundu wa anthu Koma tchimo lichititsa fuko manyazi.
— Miyambo 14:34

Lemba ili la m' buku la Miyambo lili ndi choonadi chachikulu chomwe chimapitilira tanthauzo lake laumulungu m' chilankhulo cha Chihebri. Mosakayikira, Mulungu amakondwera ndi kudalitsa mitundu ndi anthu amene amatsatira chilungamo ndi makhalidwe abwino. Koma mbali inayi, uchimo ndi wobwezeretsa m' mbuyo ndipo umabweretsa manyazi ndi chitonzo kwa anthu onse. Pamene tikukhala m' dziko limene uchimo uliponseponse ndi kusalungama kuliponseponse, tingapeze chiyembekezo m' chisomo chaumulungu chimene chimaposa mphamvu ya uchimo.

Mutu wachigawo chino ndi "Zovala za Chilungamo." Nthawi ina ndili kuyenda kokatumikira, ndinalandira masomphenya ndi uthenga wonena za "Mkwatibwi wa Khristu." Masomphenya amenewa anakulitsa kumvetsetsa kwanga kwa Mpingo monga mkwatibwi wa Khristu, kuonetsera kukongola ndi chiyero chake m' kuunika kwakukulu. Pemphero langa ndi lakuti phunziro ili likhudze wowerenga aliyense ndi kuwatsogolera kumvetsetsa bwino chilungamo chenicheni. Mulole Mzimu Woyera achite zomwe mau sangakwanitse.

Mpingo, umene umafaniziridwa ngati mkwatibwi, ukuitanidwa kukhala woyera, wopatulika, wosadzidetsa ndi wokonzekera kubweranso kwa Ambuye. Mpingo sichinthu chongoyerekeza koma ndi gulu la okhulupirira. Choncho, wokhulupirira aliyense ayenera kukongoletsedwa ndi chilungamo cha Mulungu. Ngakhale kuti pali mikangano ya tanthauzo la uchimo ndi chikhalidwe cha zadziko, ndipo pali mitsutsano pa muyeze wa chiyero wa Mpingo, kodi sitingaima kaye ndi kufunafuna masomphenya aumulungu a mkwatibwi wa Khristu? Tiyeni tiike pambali kwa kanthawi pang'ono chabe, malingaliro, maganizo, zikhumbitso ndi miyambo yathu ndi kutsegula mitima yathu ndi malingaliro athu ku Mau ndi Mzimu pamene ife tikufunafuna vumbulutso lalikulu la chilungamo.

Kodi Mulungu amafuna kuchita chiyani m' mitima yathu ndi m' miyoyo yathu? Ngati tapulumutsidwa, ndife gawo la Mpingo wake. Poganzira zimenezi, kodi tiyenera kukhala ndi moyo ndi khalidwe lotani? Kawirikawiri mikangano imachepa pamene tikuiona kupyolera mu lingaliro la chilungamo cha Mulungu. Monga mkwatibwi wa Khristu, cholinga chathu chiyenera kukhala kukondweretsa Mulungu ndi kupewa zochita ndi zimene zimapangitsa kuti tiipitsidwe ndi chilakolako cha thupi, chilakolako cha maso, ndi kudzikuzwa kwa moyo.

Pamene tikuona kukongola kwa chilungamo, pali kudekha ndi kulimbana kwa ife pamene tikuunguza miyoyo yathu ndi kutsimikizira kuti ikugwirizana ndi chiyero cha Mulungu. Tonse tili ndi zofooka, koma cholinga chathu chiyenera kukhala ngati Khristu, kulola Mzimu Woyera kutikonza ndi kutiumba. Monga momwe chidetso chaching'ono chingaitse kapu yonse ya madzi, kupanda chilungamo pang'ono kungaononge mzimu wathu.

Tiyeni tione chiyero cha mkwatibwi ndi kufunafuna moona mtima kukhala moyo wolungama ndi wovomerezeka pamaso pa Mulungu.

Michael W. Smith

October 2024

Kapena simudziwa kuti osalungama sadzalandira Ufumu wa Mulungu?

(1 AKORINTO 6:9-10)

Adama	Achigololo	Osilira	Olanda
Olambira mafano	Akuba	Zidakwa	
Ogona ndi amuna kapena akazi anzaa			



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

KUSALUNGAMA



Kalozera pophonzira Baibulo

Mutu: Chilungamo

Kuwerenga Malemba:

Wadza ukwati wa Mwanawankhosa; ndipo mkazi wake wadzikonzera...avale bafuta wonyezimira woti mbu; pakuti bafuta ndiye zolungama za oyera mtima. — Chivumbulutso 19:7-8

Tanthauzo: Chilungamo ndicho “kuchita zinthu mogwirizana ndi lamulo laumulungu kapena la makhalidwe abwino. Kukhala womasuka ku kupanda kulakwa kapena kuchimwa” (*Merriam-Webster*). “Chiphunzitso chokhudza njira imene munthu angapezere mkhalidwe wovomerezeka ndi Mulungu. Umphumphu, ukoma, chihero cha moyo, kulungamitsidwa, kulondola kwa kaganizidwe, kumva, ndi kuchita” (*Thayer*).

Mwachidule: Mpingo uli ngati mkwatibwi amene akudikirira kubwera kwa mkwati wake. Ayenera kuvala zovala zoyera zachilungamo. Ana a Mulungu ayenera kukhala olungama ndi moyo waumulungu, okonzekera kubweranso kwa Yesu Khristu.

I. Mkwatibwi wa Khristu

- A. Chivumbulutso 21:1-2 Wokongoletsedwa kwa mwamuna wake.
- B. Chivumbulutso 21:9-11 Mkwatibwi, mkazi wa Mwanawankhosa.
- C. Aefeso 5:25-27 Wopanda banga kapena khwinya.
- D. 2 Akorinto 11:2 Namwali woyera.

II. Chovala choyera cha oyeramtima

- A. Chivumbulutso 19:7-9 Bafuta woyera ndiye chilungamo.
- B. Chivumbulutso 3:4-5 Wavekedwa zovala zoyera.
- C. Chivumbulutso 7:9 Oyeramtima Kumwamba atavala miinjira woyera.

III. Tumikirani Yehova m'chilungamo

- A. Luka 1:74-75 Tumikirani Mulungu m'chilungamo.
- B. 1 Yohane 3:6-8 Iwo amene akhala mwa Khristu sachimwa.
- C. Aroma 6:18-19 Atumiki a chilungamo.
- D. 1 Akorinto 6:9-10 Ntchito zosalungama.

IV. Kuitanidwa ku chilungamo

- A. Mateyu 6:33 Funafunani chilungamo chake.
- B. 1 Timoteo 6:11 Tsatani chilungamo.
- C. Aefeso 4:24-25 Valani umunthu watsopano.

V. Mwa chikhulupiro osati mwa chilamulo

- A. Agalatiya 2:16 Osalungamitsidwa ndi ntchito za lamulo.
- B. Aroma 5:1 Kulungamitsidwa mwa chikhulupiro.
- C. Aroma 5:18-21 Olungama mwa Khristu.

VI. Chilungamo chamunthu sichokwanira

- A. Afilipi 3:7-9 Osati chilungamo cha munthu.
- B. Aroma 10:3-4 Akhazikitse chilungamo chaochao.
- C. Yesaya 64:6 Zilungamo zathu zili ngati nsanza zodetsedwa.
- D. Tito 3:5 Osati mwa ntchito za chilungamo.
- E. Mateyu 5:20 Kuposa cha Afarisi.
- F. Mateyu 23:27-28 Maonekedwe akunja.

VII. Kulimbikitsidwa ku chilungamo

- A. 1 Akorinto 15:34 Dzukani ku chilungamo.
- B. 2 Timoteo 3:16 Malemba ali olangiza.
- C. Yesaya 28:17 Chingwe ndi chingwe choongolera.
- D. 1 Akorinto 6:9-10 Osalungama sadzalandira cholowa.

VIII. Mkwatibwi anasiyana ndi hule

- A. Chivumbulutso 12:1 Mkazi wovekedwa dzuwa.
- B. Chivumbulutso 17:1-6 Hule lalikulu.
- C. Yesaya 1:21-22 Mzinda wokhulupirika wasanduka hule.

IX. Malonjezo kwa olungama

- A. 1 Petro 3:12 Makutu amamva mapemphero awo.
- B. Machitidwe 10:35 Analandiridwa ndi Mulungu.
- C. 1 Petro 3:14 Odala muli inu.
- D. Mateyu 5:6 Odala ali iwo.
- E. 2 Timoteo 4:7-8 Korona wa chilungamo.

X. Zovala zopanda banga

- A. 2 Petro 3:10-11 Kodi ndi anthu otani.
- B. 2 Petro 3:14 Opanda banga ndi opanda chilema.

Kumaliza

Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama lye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse.

— 1 Yohane 1:9



ZOVALA ZA Chilungamo

Mkwatiyo analowa m'chipindamo nayang'ana mkwatibwi wake wonyezimira, amene anali kuyembekezera mwachidwi kuti adzagwirizana kwamuyaya ndi wachikondi wake. Atavala mkanjo woyera, wonyezimira, wopanda chilema chilichonse, nkhope yake inawala pamene ankalandira mkwati wake ndi chisangalalo. Nthawi yomwe anthu ankayembekeza kwa nthawi yaitali inafika.

“Chilungamo cha oyera mtima chimatheka chifukwa cha ntchito yopepesera machimo ya mwazi wa Yesu Khristu ndi chikoka choyeretsa cha Mzimu Woyera.”

Mkwatibwi wa Khristu

Yohane anali ndi masomphenya ofananawo a Mpingo wa Mulungu, limenenso limaimira kuti mkwatibwi wokonzekera kukumana ndi mkwati wake: “Ndipo ndinaona mzinda woyerawo, Yerusalemu watsopano, ulikutsika Kumwamba kwa Mulungu, wokonzeka ngati mkwatibwi wokometsedwera mwamuna wake.” (Chivumbulutso 21:2). Masomphenya amenewa

akuonetsa oomboledwa monga mzinda wokongola wa Yerusalemu komanso ngati mkwatibwi: “Idza kuno, ndidzakuonetsa mkwatibwi, mkazi wa Mwanawankhosa” (v. 9). Monga mkwatibwi wodzikongoletsa yekha kuti akondweretse mwamuna wake, Mpingo woona umafuna kukondweretsa Khristu yekha. Khristu anakonda Mpingo, mkwatibwi wake, koterokuti Iye anapereka moyo wake “kuti akampatule, atamyeretsa...kuti Iye akadziikire yekha Mpingo wa ulemerero, wopanda banga, kapena khwinya, kapena kanthu kotere; komatu kuti akhale woyera, ndi wopanda chirema” (Aefeso 5:26-27). Paulo ananena za mkwatibwi wa Khristu monga “namwali woyera” wopalidwa ubwenzi ndi mwamuna mmodzi, amene ali Khristu (2 Akorinto 11:2).

Ambuye atsegule maso akhungu kuti aone kukongola kwenikweni kwa Mpingo umodzi wa Mulungu. Monga mkwatibwi amene ali namwali, Mpingo uyenera kukhala womvera kwa Khristu yekha ndi kuyang'ana maso ake pa Iye yekha. Chikhumbo chake chiyenera kukhala ndi moyo ndi kuchita zinthu mogwirizana ndi Mwana wa Mulungu.

Ukwati wa Mwanawankhosa

Ubale womaliza wa Khristu ndi Mpingo kumapeto kwa nthawi umaonetsedwa ngati ukwati. Lemba la Chivumbulutso 19:7-8 limanena za kukongola

kwa mkwatibwi: “Tikondwere, tisekerere, ndipo tipatse ulemerero kwa Iye; pakuti wadza ukwati wa Mwanawankhosa; ndipo mkazi wake wadzikonzera. Ndipo anampatsa iye avale bafuta wonyezimira woti mbu; pakuti bafuta ndiye zolungama za oyera mtima.” Mkwatibwi, amene wadzikonzekeretsa, wavala bafuta woyera, wonyezimira, akuimira chilungamo—chiyero, ukoma, makhalidwe abwino, ndi zonse zoyenera ndi zolungama. Chilungamo ndi chikhaliidwe chamkati ndi khalidwe lomwe limaperekedwa ndikuvomerezedwa ndi Mulungu. Wokhulupirira aliyense akuyenera kudzikonzekeretsa yekha monga mkwatibwi, kukhala ndi moyo wokondweretsa Mulungu. Chilungamo cha oyera mtima chimatheka chifukwa cha ntchito yopepesera machimo ya mwazi wa Yesu Khristu ndi chikoka choyeretsa cha Mzimu Woyera.

Ambiri amene amadzinena kuti ndi Akhristu adetsa zovala zao ndi uchimo komanso zadziko, koma anthu oona a Mulungu akudzikonzekeretsa okha mu chiyero ndi umulungu. Amene agonjetsa uchimo “adzavekedwa malaya oyera” (Chivumbulutso 3:4-5), chizindikiro cha chiyero ndi kusalakwa. Okhawa amene amasunga zovala zao zauzimu kukhala zoyera padziko lapansi pano adzalowa mu ulemerero wamuyaya, pakuti ndi oyera okha amene adzakhale Kumwamba (Chivumbulutso 7:9).

Oyera mu mtima

Yesu anadza napereka moyo wake nsembe kuti anthu ake amtumikire “m'chiyero ndi chilungamo” (Luka 1:75). Chilungamo chenicheni si chakunja chabe, koma chiyero cha mumtima. Anthu a Mulungu ayenera kukhala m'chilungamo. 1 Yohane 3:6-8 amaphunzitsa momveka bwino kuti amene amakhala mwa Khristu sakhala mu uchimo, chifukwa Khristu anabwera kudzaononga ntchito za Mdierekezi. Okhulupilira amaitanidwa kuti akhale ndi moyo monga Khristu adakhalira - mu chilungamo. “Munakhala akapolo a chilungamo... tsopano perekani ziwalo zanu zikhale akapolo a chilungamo kuti zichite chiyeretso.”

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

Kuitanidwa ku chilungamo

Mobwerezabwereza lemba limatchula anthu kuti atsatire chilungamo pa zokondweretsa zosakhalitsa za dziko lapansi ndi zilakolako za thupi. Yesu anati funafunani “ufumu wa Mulungu, ndi chilungamo chake” (Mateyu 6:33). Akhristu akulimbikitsidwa kuthawa uchimo ndi “kutsata chilungamo, umulungu, chikhulupiriro, chikondi...” (1 Timoteo 6:11). Anthu ambiri amanena kuti amatsatira Khristu pamene iwo akukhala m'moyo wauchimo ndi m'chisalungamo. Paulo akulimbikitsa mpingo pa Aefeso 4:24-25 kuti: “nimuvale munthu watsopano, amene analengedwa monga mwa Mulungu, m'chilungamo, ndi m'chiyero cha choonadi.” Chilungamo chimadza kupyolera mu ntchito ya umulungu ndipo chimakhazikika mu zisankho ndi malingaliro athu a tsiku ndi tsiku.



Kuitanira ku
chiyero uku
kumakhudza
mbali zonse za
moyo wathu—
mzimu wathu,
maganizo athu,
zokhumba zathu,
mau, zochita...”

Uthenga wa Paulo kwa Mpingo ukadali wofunikira lero lino: “Ukani molungama” (1 Akorinto 15:34). Ambiri ali m'tulo tautimu, akulola kuti zovala zao ziipitsidwe ndi dziko. Akhristu amafunika kuzindikira kuti adziwe chimene chili cholungama ndi chosalungama. Malemba anaperekedwa kaamba ka “chilangizo cha m'chilungamo” (2 Timoteo 3:16), komabe ambiri amanyalanyaza mau a Mulungu, akumagonjera ku zilakolako za mbadwo woipa uwu. Choonadi chimaulula chinyengo cha mdani, ndipo chiweruzo chiyenera kukhala chingwe choongolera ndi chilungamo (Yesaya 28:17) chimene zinthu zonse zimayesedwa.

Mkwatibwi komanso hule

Masomphenya a Yohane mu buku la Chivumbulutso amasiyanitsa mipingo iwiri. Pa mutu 12, mkwatibwi weniweni wa Khristu akuonetsedwa kukhala wovekedwa ndi dzuwa, lovala choonadi ndi chiyero. Pa mutu 17, akulongosola za mtundu wina wa mkazi, wovala chibakuwa ndi chofiira, wovekedwa ndi golidi ndi miyala yamtengo wapatali. Mkazi ameneyu, amene anachita dama lauzimu, ankatchedwa hule. Iye akuimira Babiloni, chizindikiro cha zipembedzo zachikhristu zonyenga zimene, pamene zimalengeza Khristu monga Ambuye, zimakhala zodetsa ndipo zimalola uchimo. Iye amaipitsa chiphunzitso choyera cha Baibulo kuti asangalatse anthu. Kodi inuyo muli a mpingo utiwo - umene uli wangwiwo ndi wopanda banga, kapena wooneka wokopa ndi zolankhula zake zabwino, ndi madongosolo ake, ndi chifundo chake, koma ukulekerera uchimo ndi chidetso?

Yesaya 1:21-22 akuwulula za ana a Israele amene poyamba anali mzinda wokhulupirika koma tsopano unasanduka hule. Ngakhale kuti panthawi

ina chilungamo ndi chiweruzo zinkakhala mkati mwa malinga awo, iwo anayamba kusakaniza kupembedza mafano ndi chiphunzitso chonyenga ndi choonadi. Ambiri odzitcha Akhristu lero lino ali mumkhalidwe wofananawo, wosakhulupirika kwa mkwati ndipo savalanso chilungamo cha Mulungu.

Malonjezo kwa olungama

Kukhala ndi moyo utavala miinjira ya chilungamo ndi moyo wodabwitsa ndi wodalitsika. Malonjezo ambiri amaperekedwa kwa olungama. “Pakuti maso a Ambuye ali pa olungama, ndi makutu ake akumva pembedzo lawo” (1 Petro 3:12). “Iye amene amamuopa [Ambuye] ndi kuchita chilungamo alandiridwa ndi Iye” (Machitidwe 10:35). “Ngati mumva zowawa chifukwa cha chilungamo, odala inu” (1 Petro 3:14). “Odala ali akumva njala ndi ludzu la chilungamo: chifukwa adzakhuta” (Mateyu 5:6). Chofunika koposa, pali korona wa chilungamo ndi moyo wosatha Kumwamba wolonjezedwa kwa iwo amene amenya nkondo yabwino ndikukhala molingana ndi Mau a Mulungu (2 Timoteo 4:7-8).

Kulangizidwa za chilungamo

Yesu akubwera posachedwa, ngati mbala usiku. Dzikoli lidzaonongedwa, ndipo anthu onse adzaimirira pamaso pa mpando wa Mulungu wakuweruza. Podziwa izi, ndi kudziwa kuti Khristu akubwerera anthu angwiwo ndi oyera, “Muyenera kukhala anthu otani nanga m'mayendedwe onse opatulika ndi m'chipembedzo” (2 Petro 3:11). Kuitanira ku chiyero kumeneku kumakhudza mbali zonse za moyo wathu—mzimu wathu, maganizo athu, zokhumba zathu, mau, zochita, zinthu zimene timamvetsera ndi kuonera, zovala zimene timavala, malo amene timapitako, maubale athu, ngakhalenso ziphunzitso zimene timakhala nazo. Kodi zinthu izi zikugwirizana ndi chilungamo m'moyo wanu? Kodi iwo ali angwiwo ndi oyera? Kodi zimasonyeza mkwatibwi woyera wa Khristu? Petro akupitiriza mu vesu 14 kuti: “Chitani changu kuti mupezedwe ndi iye mumtendere, opanda banga ndi opanda chilema.”

Kodi chovala chanu chaukwati chili chotani? Kodi pali makwinya a dziko lapansi kapena mawanga a uchimo? Kodi mukudzikongoletsa nokha kuti mukondweretse Khristu kapena kudzikondweretsa nokha ndi iwo omwe akuzungulirani? Ndizotheka kukhala ndi moyo wolungama kudzera mu mphamvu ya Yesu Khristu.

Ngati simunavekedwe ndi chilungamo cha Mulungu, mudzipereke nokha kwa Mulungu ndikupempha ntchito yake yaumulungu mu mtima mwanu. “Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse” (1 Yohane 1:9). Tiyeni tikhale moyo tsiku lililonse okonzeka kukumana ndi Khristu, pakuti Iye akudza posachedwa. ■



Funso: Kodi munthu amayesedwa wolungama amene amasunga ziphunzitso za mpingo?

Funso limeneli limafika pamtima pa tanthauzo la chilungamo chenicheni. Kawirikawiri mtumwi Paulo ananena za nkhanayi pamene ankaunguza za mikangano imene inalipo pakati pa Akhristu Achiyuda ndi akunja ongotembenuka kumene. Ayuda ambiri ankafuna kulungamitsidwa potsatira miyambo ndi malamulo a m'Chilamulo cha Mose.

“Chilungamo chimapezeka kudzera mwa chikhulupiriro mu ntchito ya umulungu ya Khristu, osati potsatira mndandanda wa malamulo.”

Chimodzimidzi, anthu ena mu mpingo masiku ano amayang'ana ku malamulo ndi ziphunzitso monga njira ya chilungamo.

Komabe, Paulo akunenetsa momveka bwino lomwe kuti chilungamo

chenicheni sichingapezeke kudzera mu zochita zathu. Pa Agalatiya 2:16 amati: “Podziwa kuti munthu sayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo, koma ndi chikhulupiriro cha Yesu Khristu. pakuti palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo.”

Mu dongosolo la Mulungu, chilungamo chimapezeka kudzera mwa chikhulupiriro mu ntchito ya umulungu ya Khristu, osati potsatira mndandanda wa malamulo. Ngakhale

kuti malamulo kapena ziphunzitso zikhale zabwino bwanji, sizingabweretse chipulumutso. Kulungamitsidwa—kunenedwa kukhala “wosalakwa” kapena “wolungama” pamaso pa Mulungu—sikuchokera ku zoyesayesa zathu. M'malo mwake, timayesedwa olungama ndi chikhulupiriro, pakuti chilungamo chimakhala chochokera mu mtima osati zochita zakunja.

Anthu akhoza kupemphera, kupereka nsembe, kutamanda, kupereka, kuvala moyenera, ndi kuchita zinthu zina zabwino, koma zochita zokhazo sizingasinthe mmene mtima ulili. Ngakhale munthu amene sakhulupirira Mulungu angathe kuchita zimenezi. Ndi kupyolera mu ntchito yaumulungu yokha imene munthu angayesedwe kukhala “wolungama” pamaso pake. Aroma 5:1 amatiphunzitsa kuti, “Chifukwa chake popeza tayedwa olungama ndi chikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.” Pambuyo pake pa Aroma 5:18-21, Paulo akufotokoza kuti kudzera mu kumvera kwa Khristu ambiri amayesedwa olungama. Chilungamo ichi ndi kusandulika kwa mtima kumene kumabwera kudzera mu mphamvu ya mwazi ndi ntchito ya Mzimu Woyera.

Ngakhale kuti ntchito zabwino ndiponso kumvera Mau a Mulungu zimachokera mu mtima wosinthika, ntchito zimenezi pazokha sizibweretsa chilungamo cha Mulungu; koma zili chipatso cha chilungamo, osati muzu wake.

Nkofunika kuvomereza kufunikira kwa ntchito zabwino. Munthu amene wavekedwa chilungamo cha Mulungu adzafuna kulemekeza lye m'moyo watsiku ndi tsiku, kuyenda m'chiyero ndi kutsata kukula kosalekeza m'chisomo cha Khristu. Komabe, tiyenera kusamala kuti tisadalire ntchito zimenezi monga maziko a ubale wathu ndi Mulungu.

Chilungamo sichimabwera chifukwa tasunga ziphunzitso za mpingo. Chimabwera kudzera mu chikhulupiriro cha mphamvu yakusintha ya Khristu, yomwe imatsogolera ku ntchito zabwino zochokera mu mtima wolungama.



“Zolungama zathu zonse zili ngati nsanza zodetsedwa.” —Yesaya

“Ngati chilungamo chanu sichiposa cha alembi ndi

Afarisi, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba.” — Yesu

“Osati mwa ntchito zachilungamo zimene ife tazichita.” —Paulo

“Inunso muonekera olungama pamaso pa anthu, koma

m'kati muli odzala ndi chinyengo ndi kusayeruzika.” —Yesu

“Ndipo ndipezeke mwa iye, wopanda chilungamo changa.” —Paulo



KODI MUKUDZIWA?

Kafukufuku akuonetsa kuti kutsata zizolowezi zamakhalidwe abwino komanso zauzimu kumatha kukhudza thanzi lamalingaliro, kuchepetsa nkhwana komanso kulimbikitsa thanzi labwino. Anthu omwe amachita zachipembedzo kapena zauzimu nthawi zambiri amafotokozeka kutsika kwapang'onopang'ono komanso thanzi labwino. [Koenig, Harold G. Chipembedzo, Uzimu, ndi Thanzi. *International Journal of Psychiatry in Medicine*, 2008]



Mau a Nyengo Yake

KUIMBA M'MAVUTO

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

Pakati pa usiku, Paulo ndi Sila analinkupemphera, naimbira Mulungu nyimbo, ndipo a m'ndendemo analinkuwamva. — Machitidwe 16:25

Pamene anali paulendo wokalalikira uthenga wabwino, akuchita ntchito ya Mulungu, Paulo ndi Sila anagwidwa, anawavula zovala, nakwapulidwa ndi zikwapu zambiri ndi kuponyedwa m'ndende. Pakati pa usiku, mapazi awo atamangidwa m'zigologolo ali m'ndende, anthu awa ali magazi chuchuchu anapemphera ndipo kenaka anayamba kuimba nyimbo zotamanda Mulungu.



Panachitika chivomezi chachikulu; zitseko za ndende zidatseguka, ndipo am'ndende aja adamasuka. Pamene chozizwitsa ichi chinachitika usiku umenewo, abale amenewa anali kuimba m'chisautso chao chiombolo chao chisanadze. Ambuye atithandize ife kupeza malo achete mu ubale wathu ndi Iye kumenenso ife tingathe kuimba ngakhale tikukumana ndi zovuta za moyo.

[Zolembe zili m'munsimu zafotokozedwa kuchokera ku nkhani yolembedwa ndi CW Naylor mu *Chinsinsi cha Mtima Woimba*.]

Moyo wadzaza ndi mavuto, zowawa, ndi zokhumudwitsa. Ngati tiyembekezera moyo wopanda mavuto kuti ukhale wosangalala, sitidzapeza chimwemwe chochepa. Chimwemwe chenicheni sichimabwera chifukwa cha kumasuka kapena kusowa zopinga, koma kuzigonjetsa. Nthawi zambiri, chisangalalo chenicheni chimachokera ku miyoyo yomwe imapirira zovuta zambiri.

Pa 2 Akorinto 7:4, Paulo akulemba kuti: “ndidzazidwa nacho chithonhozo, ndisefukira nacho chimwemwe m'chisautso chathu chonse.” Wolembe Salmo nayenso akuvomereza zimenezi, kuti: “Ndidzakondwera ndi kusangalala m'chifundo chanu: Pakuti mudapenya zunzo langa; Ndipo mudadziwa mzimu wanga mu nsautso yanga” (Salmo 31:7). Kudziwa kuti Mulungu alipo panthawi yamavuto kumabweretsa mtendere.

Yesu akudziwa zowawa zanu zonse—zosautsa ndi zovuta zilizonse. Khulupirirani chisomo chake, ndipo posachedwa, mtima wanu udzadzazidwanso ndi nyimbo, pakuti mitambo idzapita.

Mavuto amatiphunzitsa kuti tiimbe nyimbo yatsopano, imene imafunika kulimba mtima komanso kukhulupirira. Izi ndi nyimbo za kudalira, kukhulupirira ndi chiyembekezo cha chipambano chamtsogolo. Izi ndi nyimbo zoyamikira chifundo cha Mulungu chakale. Ngakhale kuti ndi zovuta kuphunzira, nyimbo zimenezi zingabweretse chisangalalo chachikulu kuposa zimene zimaimbidwa m'nthawi imene zinthu zili zokoma, chifukwa zimachokera ku chikhulupiriro chozama. Ngakhale titakumana ndi mayesero otani, ngati tidalira Mulungu, tikhoza kuimba nyimbo pa nthawi ya mavuto. ■

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

